

NYA_TTB_1098_SCRIPT

1 Yohane : 2:23-29

Mutu : Kumdziwa Yesu Kristu

Landirani moni wa Kumwamba inu wokonedwa anzanga apaulendo. Lero tiyamba ndi mau apa Mateyu 12:33, pamene Ambuye Yesu akuti, “Ukakoma mtengo, chipatso chake chomwe chikoma; ukaipa mtengo, chipatso chake chiipa; pakuti ndi chipatso chake mtengo udziwika.”

Mupologalamu yatha tinali kusanthula 1 Yohane 2:19-22, momwe timapitiliza kuona za wokana/wotsutsa Kristu. Ndipo lero pa 1 Yohane 2:23-29, tikambirana nkhani ya kumdziwa Yesu Kristu.

23.Yense wakukana Mwana alibe Atate; wobvomereza Mwana ali ndi Atatenso.

Tiyeni pano tiyambe ndi mau akuti pamene inu munena kuti mumakhulupirira Mulungu, koma mukana umulungu wa Kristu, zikutanthauza kuti inu simukhulupirira mwa Mulungu, wa m’Baibulo. Ndikunena mau amenewa chifukwa Mulungu wa m’Baibulo ndiye amene adatuma Mwana wake m’dziko lino kudzafera machimo anthu. Ndiye popeza Mwana ndiye Mulungu

amene, kotero kuti ndiyekhayo amene akanapereka nsembe yokwanirakwa Mulungu chifukwa cha machimo athu. Pachifukwa chimenechi tikunenetsa kuti “mzimu uli wonse umene ubvomereza kuti Yesu Kristu anadza m’thupi, uchokera mwa Mulungu; ndipo mzimu uli wonse umene subvomereza Yesu suchokerakwa Mulungu; ndipo uwu ndiwo mzimu wa wokana Kristu umene mudamva kuti ukudza; ndipo ulimo m’dziko lapansi tsopano lomwe” (1 Yohane 4:2-3).Tere tikunena kuti Yesu akanakhala munthu wina osakhala Mulungu ndiye kuti akanakhala wochimwa.Ndiye monga pali m’gwirizano weni-weni pakati pa Atate ndi Mwana, zikutanthauza kuti sipangakhalenso kutsutsana m’chiphunzitso ndi m’chidziwitso. Kutanthauza kuti pamene inu muli ndi chidziwitso choona cha Mwana, muli ndi chidziwitso choona cha Atate.Apa, ndipo pamene inu mungakhale ndibvumbulutso kapena chidziwitso choona cha chikristu chanu.

24.Koma inu chimene munachimva kuyambira pachiyambichikhale mwa inu. Ngati chikhala mwa inu chimene mudachimva kuyambira pachiyambi, inunsomudzakhalabe mwa Mwana ndi mwa Atate.

Pamene Yohane akunena kuti “Koma inu chimene munachimva kuyambira pachiyambichikhale mwa inu.” Tsono mau akuti “Pachiyambi” m’l Yohane akuchokera kutari m’mbuyomu momwe akunena za kubadwa kwa Kristu. Kotero kuti pamene akunena mau akuti, “chimene mudachimva kuyambira pachiyambi” akunena kuti adamvazakubadwakwa Yesu, moyo wake, chimene adamva za imfa ndi kuuka kwake. Mwanjira ina Yohane akuwauza kuti ayenera kusunga chomwe adamva kuchokera pachiyambi pomwe Atumwi adayamba kulalikira Uthenga Wabwino.

Ndiye tamvani Yohane akuti, “Ngati chikhala mwa inu chimene mudachimva kuyambira pachiyambi, inunsomudzakhalabe mwa Mwana ndi mwa Atate.” Apa Yohane, akupereka upangiri ndi chilimbikitso kwa wokhulupirira kuti ayenera kukhalabem’chiphunzitso chomwe adamva kale. Kutanthauza kuti choonadi ndicho chinadza kale kapena kuti chinadza poyambirira kusiyana ndi ziphunzitso zonama. Ndiye upangiri ukunena kuti choona chokhudza Kristu, chomwe chinalalikidwakwa akristu, sichiyenera kusinthitsidwa ndi chiphunzitso Chatsopano chabodza ayi.

Wokondedwa anzanga apaulendo nkhani iyi, ikuti ndibwino kukhala ndi chikhulupiriro chomwe ndi cha moyo chomwe chimakhazikika pa Iye amene anadza m'dziko lapansi zaka zoposa 2,000 m'mbuyomo. Tikunena panthawi yomwe Ambuye Yesu anadza mwakubadwa monga tiwerenga pa Yohane 1:14, pamene akuti, "Ndipo Mau anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife, ndipo tinaona ulemerero wake, ulemerero wongawobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi chisomo ndi choonadi." Awa, ndiwo mau amene ndi amphamvu kwambiri chifukwa ndiwo amene akutsimikiza za kupezeka kwa Mulungu pakati pa anthu. Tamvani Yohane 1:18, akuti, "Kulibe munthu anaona Mulungu nthawi zonse; Mwana Wobadwa yekha wakukhala pa chifuwa cha Atate, Iyeyu anafotokonzera."Tere ndimau awa okha, amene akufotokonzera kuti tikhoza kum'dziwa Mulungu kupyolera mwa Ambuye Yesu Kristu. Tsono mundime ino Yohane sakunena za momwe ifetingapezere moyo kudzera m'chikhulupiriro mwa Yesu ayi, koma akukamba za moyo wachisangalalo ndi kukhala m'chiyanjano ndi Mulungu wathu. Kodi inu muli wotsimikiza mtima kuti mulinayem'chiyanjano Mulungu?

25.Ndipo ili ndi lonjezano Iye anationjezera ife, ndiwo moyo wosatha.

Pano Yohane akunena za lonjezano lomwe Mulungu adaperekakwa wokhulupirira onse. Ili ndilo lonjezanoloyenera monga mwaukulu wake, mphamvu ndi kukomamtima kwake.Ili, ndilo lonjezano la moyo wosatha, lomwe wina aliyense sangapereke koma Mulungu yekha, mwa Mwana wake yekha. Kutsimikiza kuti Mulungu amaika chitsimikizo chonse mwa Mwana wake, pamene akulonjeza moyo wosatha kwa onse amene apitiliza kukhala m'choonadi cha moyo wosatha. Kutanthauza kuti Mulungu amapereka mtundu wokhawuwa moyo wosatha, kwa iwo akukhazikikam'choonadi. Tikunena kuti ngati inu mungataye moyo ndiye kuti mukutaya moyo wosatha.

26.Izi ndakulemberani za iwoakusokeretsa inu.

Tsono mau akusokeretsaali ndi tanthauzo limodzi kumoyowathupindiwauzimu. Tikunena kuti pamene munthu apanga inu kuchoka pa choonadi, ndiye kuti akukusokeretsani. Ndiye Mtumwi Yohane akunena kuti m'masiku ake, analipo anthu ena amene amakana Atate ndi Mwana wake Yesu Kristu. Awa,

ndiwo anthu amene anayamba kusokeretsa akristu amene anagwira kale choonadi. Ndiye Yohane akuwalangiza kuti iwo sayenera kubvutika ndi kupereka mayankho ochuluka, koma kungogwiritsitsa kuti Mulungu adawalonjeza moyo wosatha, pakuika chikhulupiriro chawo mwa Yesu Kristu kotero kuti sipafunikansokuonjezapo china chilichonse ayi.

Iye amanena mau amenewa chifukwa panadza anthu ena amene amanena kuti ali ndi chidziwitso chochuluka kuposa chomwe akristu anali kudziwa. Tere ichi, ndicho chobvuta china pakati pa akristu chifukwa alipo ena amene amadzitenga kuti ndiwo ali ndi chidziwitso chokwanira kuposa wina aliyense. Tsono ndifuna kunenetsa kuti pamene inu mufikapamzere umenewu, ndiye kuti mwafikapodzikweza. Kumbukirani kuti “Kunyada kutsogolera kuonongeka” (Miyambo 16:18). Ndiye tikunena kuti pamene inumukula m’chisomo ndi m’chidziwitso cha Mulungu, mudzakhala ndi moyo wofanana ndi wa Yohane m’Batizi pa Yohane 3:30, amene adanena kuti, “Iyeyo ayenera kukula koma ine ndichepe.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunena moona mtima kuti, pamene munthu apitiliza kusanthula mau a Mulungu

ndipomwe amadziona kuperewera kwambiri. Tikunena kuti pamene inu muzamamkusanthula mau a Mulungu, ndipamene mumazindikira kuti simudziwa kanthu. Poyamba pamoyo wanga wachikristu, ndimaganiza kuti ndimadziwa zinthu zambiri, koma pano pamene ndinapatsidwa mwayi wosanthula mau a Mulungu ndafikapozindikira kuti sindidziwa kanthu. Kutanthauza kuti mwana wa Mulungu akanali ndi mtunda waukulu kuti afikepomdzwitsitsa Kristu. Ichi, ndichifukwa chake inu ndi ine, tiyenera kutenga ntchito yosanthula mau a Mulungu kukhala chinthu chofunika kwambiri m'moyo mwathu. Tere ndichifukwa chake Mtumwi Yohane akunena kuti safuna kuti akristu akhale wodzitamandira ndi kunena kuti afikapo ayi, koma kuti angokhazikika pa malonjezano a Mulungu.

27. Ndipo inu, kudzoza kumene munalandira kuchokera kwa Iye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni; koma monga kudzoza kwake kukuphunzitsani za zinthu zonse, ndipo kuli koona, sikulibodza ayi, ndipo monga kudaphunzitsa inu, mukhale mwa Iye.

Tiyeni poyamba tione tanthauzo la liwu la “kudzoza.”Liwu limeneli limatanthauza kupaka kapena kumata.Kunena kuti nthawi zina pamene munthu adwalachifine, amatengamankhwala okhala ngati mafuta odzola ndiye munthu amapakapakhosi kapena pamtima.Kutanthauza kuti pamene inu muchita chimenechi, ndiye kuti muli kudzidzoza nokha.

Tsono pamene tibwerera m’Chipangano Chakale, tipeza kuti mwakulamulidwa ndi Mulungu, ansembe a Israyeli anali kudzozedwa ndi mafuta. Ndiye mafuta amenewa pathupi la munthu anali kuonetsa kuti munthuyu wadzazidwa ndi Mzimu Woyera kuti atumikirepaudindo wina.Uku, ndiko kudzoza kumene inu ndi ine tidziwa lero lino. Koma kudzoza kumeneakunena Yohane ndikumene inu ndi ine tinalandira panthawi yomwe tinalandiridwa muufumu wa Mulungu pamene tinapulumsidwa. Tikunena kuti chinthu chimodzi chomwe chimachitika panthawi yomwe talandira chipulumutso ndi chakuti Mzimu wa Mulungu amadzoza aliyense amene wapulumutsidwa kuti akhoze kumva chifuniro cha Mulungu chomwe kale sanali kuchimvetsa.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunenetsa kuti pamene Mtumwi Yohane akunena kuti, “Ndipo inu kudzoza kumene munalandira kuchokera kwa Iye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni...” sakunena kuti inu kapena ine, sitifuna wina kuti atiphunzitsechifukwa Paulo kumpingo wa ku Aefeso 4:11, adanena kuti “Ndipo Iye anapatsa ena akhale Atumwi; ndi ena aneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa; ndi ena aphunzitsi.” Paulo akunena kuti Mulungu adapereka anthu amenewa ndi cholinga chakuti athandizire kumanga mpingo. Kutsimikiza kuti Yohane sakunena kuti ifesitifunamphunzitsi ayi, koma akutanthauza kuti Mzimu Woyera ndiye wofunika kwambiri kwa ife wokhulupirira. Ichi, ndichifukwa chake pa verse 20, adanena kuti, “Ndipo inu muli nako kudzoza kochokera kwa Woyerayo ndipo mudziwa zonse.” Ndiye tikuti udindo wina wa Mzimu Woyera ndiwo kuphunzitsa ife. Kunena kuti ndiye amene ali wokwanira kutiongoleram’choonadi chonse. Mukumbukira kuti Ambuye Yesu, Mphunzitsiwamkulu pa Yohane 14:26, ndiye adanena kuti, “Koma Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m’dzina langa, Iyeyoadzaphunzitsa inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu.” Tere tikunenetsa kuti Mzimu

Woyera ndiye adzatiphunzitsaife zinthu zonse zomwe tingakwanitsekusunga. Mwanjira ina tikunena kuti inu ndi ine, tinapatsidwa kudzoza ndi cholinga chakuti tikamvetse choona popeza munthu wachibadwidwe sangathe kulandira cha Mzimu wa Mulungu popeza ndizo zopusa (1 Akorinto 2:14). Ndiye Paulo yemweyo pa 1 Akorinto 2:9-10, akunena kuti, “Koma monga kulembedwa, zimene disosilina, ndi khutu silinazimva, nisizinalowa mu mtima wa munthu, zimene ziri zonse Mulungu anakonzeratu iwo akumkonda Iye.” Tsono ichi, ndichifukwa chake timanena kuti pamene tisanthula mau a Mulungu, tiyenera kupempha Mzimu wa Mulungu kuti atiphunzitse ndi kutitsogolera.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti Yohane akupitiliza kunena kuti, “Koma monga kudzoza kwake kukuphunzitsani za zinthu zonse, ndipo kuli koono, sikulibodza ayi.” Ndiye Ambuye Yesu pa Mateyu 24:24, akunena kuti, “Chifukwa Akristu onama adzauka, ndi aneneri onama nadzaonetsa zizindikiro zazikulu ndi zozizwa: kotero kuti akanyenge, ngati nkotheke, osankhidwa omwe.” Ndiye nkhani ikuti aphunzitsi onyenga alipo ndi cholinga chakuti akanyenge inu

wokhulupirira, koma chifukwa chakuti mkati mwanu muli Mzimu wa Mulungu amene amaphunzitsa zonse, inu mudzazindikira za chinyengo chawo kotero kuti ndikobvutakukunyengani. Tere tikunenetsa kuti aphunzitsi onyengawa sanganyenge ana a Mulungu pokha-pokha anawo amakhalangati ana a Mulungu. Ndikunena mau amenewa chifukwa Ambuye Yesu pa Yohane 10:27, ndipamene adatsindika kuti, “Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine.”Kodi inu muli ndi chidziwitso chokwanira kufikira pakuti simunganyengedwe?

28.Ndipo tsopano, tiyanakhalani mwa Iye; kuti akaonekere Iye tikakhale nako kulimbika mtima, osachita manyazi kwa Iye pa kudza kwake.

Yohane mundime ino akulimbikitsa wokhulupirira onse posatengerakukulam’chikhulupiriro chawo.Iye akuti, wokhulupirira ayenera kukhala mwa Kristu.Apa, akunena nkhani yokhala m’chiyanjano ndi Mulungu. Kutsindika kuti pamene tikhala mwa Ambuye Yesu Kristu, ndiye kuti tikukhala naye m’chiyanjano.

Tsono pamau akuti, “Kuti akaonekere Iye tikakhale nako kulimbika mtima.”Apa, akunena za nthawi yakubweranso kwa Ambuye Yesu

kachiwiri. Nkhani ikuti ngakhale Mzimu Woyera amatiphunzitsa zonse, koma sanatiululire za tsiku lakubweransokwa Ambuye. Kapena kunena kuti ngakhale ifetinadzozedwa, koma chinsinsi chakubwera kwake anachisungira kwa Iye yekha. Ndiye pachifukwa chimenechi, Mtumwi akuona kuti ndi koyenera kuti ana a Mulungu akhale m'chiyanjano ndi Ambuye Yesu Kristu nthawi zonse ndi cholinga chakuti asakadzidzimuke pakudza kwake.

Tikunena kuti ndikofunika kuti inu ndi ine, tikhale m'chiyanjanokapena kuti tiyende m'kuunika pozindikira za kubweranso kwake patsiku losadziwika. Nkhani ikuti inu ndi ine, tiyenera kukhala m'chiyanjanondi Ambuye Yesu Kristu chifukwa ndizotheka kutailira ngati ndingadziwe kuti Ambuye Yesu akubweranso m'zaka zisanu zikubwerazo. Kutanthauza kuti kuyambira pano kufikira zaka zisanu zikudzazo, ine ndikhoza kuyamba kuchoka pachifuniro cha Atate popeza ndikudziwa kuti nthawi ikanalipo. Nkhani ikuti chikhoza kukhala chinthu chabwino ngati Ambuye Yesu atadza ndi kukupezani inu muli otanganidwa kusanthula mau ake. Koma nthawi zina zimakhalazomvetsa chisoni kuti ngati Ambuye angabwere nthawi imeneyo, zikhoza kuchititsa

manyazi ndithu chifukwa timachimwa ndithu mkuganiza, mkulankhula ndi m'ntchito zathu zomwe. Apa, ndipo tikunena kuti pafunikadi chisomo chochuluka kuti nthawi zonse tizikhala ndi chithunzi chooneka bwino chakubwera kwa Ambuye Yesu nthawi ina iliyonse.

Tikunena kuti anthu ena adzakhumudwa komanso kuchita manyazi pakubwera Iye chifukwa chakukhala m'moyo wosakhulupirika. Tamvani Ambuye Yesu pa Chibvumbulutso 22:12, pamene akuti, "Taonani ndidza msanga; ndipo mphotho yanga ndiri nayo yakupatsa yense monga mwa ntchito yake." Ndipo Paulo pa 1 Akorinto 3:15, akunena kuti, "Ngati ntchito ya wina itenthedwa, zidzaonongeka zake; koma iye yekha adzapulumutsidwa; koma monga momwe mwa moto." Nkhani yonseyi ikuti anthu ambiri patsiku lobwera Ambuye Yesu Kristu kachiwiri, adzafunitsitsaatalandira mphotho, koma sadzazipeza. Tere ndichifukwa chake inu ndi ine, tiyenera kukhala m'moyo woyenera monga mau a Mulungu anena. Kodi inu, muli ndi chikhulupiriro chakuti simudzakhumudwa kapena kuchita manyazi pakubwera Ambuye Yesu?

29. Ngati mudziwa kuti ali wolungama, muzindikira kuti ali yensenso wakuchita chilungamo abadwa kuchokera mwa Iye.

Tsono pamene Mtumwi Yohane akuyamba ndime iyi ndi liwu lakuti “Ngati” sakunena kuti pali kukaikira za chiyero cha Kristu ayi. Koma akungofunakukumbutsa wokhulupirira kuti ndichinthu chodziwika kale kuti Kristu ndiye woyera. Mwanjira ina akunena kuti munthu aliyense amene ali m’chiyanjano choona ndi Kristu ayenera kukhala ndi chitsimikizo chakuti Kristu ndiye wolungama. Ndiye Yohane akunena kuti kwa wokhulupirira onse amene atsimikizadi kuti ndiwo ali m’chiyanjano ndi Kristu wolungamayu, ayenera kuzindikira kuti ndiwo amene anabadwanso mwa Kristu. Mwanjira ina Mtumwi Yohane akunena kuti inu (wokhulupirira) mukudziwa kuti Mulungu ndiye wolungama ndipo mumazindikira kuti munthu aliyense woyendam’chiyero cha Mulungu, Nayenso akhala wolungama. Kutsimikiza kuti munthu ameneyu ndiye amene anabadwanso mwa Mulungu. Kutanthauza kuti chinthu choyerachimaturutsa kapena chimabalachoyera. Mwa mau amenewa tikunena kuti Mulungu ndiye woyera kotero kuti ndiye kasupewachiyero chonse. Ndiye popeza Mulungu ndiye chitsime cha

chiyero cha munthu, zikutanthauza kuti munthuyu anapeza chiyerochi mwanjira yakubadwanso mwa Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti, uwu ndiwo umboni wokwanira umene udzaonetsa nthawi zonse kuti inu ndinu mwana wa Mulungu. Mwa mau onsewa, Yohane akunena kuti ana a Mulungu amaoneka ngati Atate awo. Ndiye ngati anawosangafanane ndi Atate awo, ndiye kuti si ana Atatewo. Kodi inu muli ndi chitsimikizo chakuti ndinu mwana wofanana ndi Atate anu?

Kwalerotilekeza pano. Ndipo tinali kusanthula 1 Yohane 2:23-29, momwe timakambirana nkhani ya kumdziwa Yesu Kristu.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!